

Kodi Yesu Amachiritsa



Odwala
Masiku
ANO?

Ndizosachita kufunsa, utumiki waukulu wa Yesu padziko lino lapansi unali wochiritsa odwala (Mateyu 9:35,36). Cholinga chake chachikulu pochiritsa odwala ndi osautsidwa sichinali kungowonetsa mphamvu zake ndi uMulungu wake ayi. Mu uthenga wabwino wa Mateyu timauzidwa kuti Yesu anali ndi chisoni chachikulu pa anthu (Mateyu 9:35,36).

Yesu anenenera kuti omtsaira lye adzapitilira kuchiritsa odwala, “Adzaika manja awo pa odwala, ndipo adzachira” (Marko 16:18). Mmautumiki onse a ophunzira a Yesu omwe alembedwa m’buku la Machitidwe a Atumwi munali zozizwitsa za machiritso mu mphamvu ya Mulungu—Machitidwe 3:6-8, 9:32-41, 5:15,16, 19:11,12. Yakobo analangiza odwala mtchalitchi kuti azilitana akuluampingo (Abusa) amene akhoza kuwapemphelera kuti achiritsidwe.

Kodi Yesu amachiritsa odwala masiku ano? Wolemba buku la Aherberi akunena kuti “Yesu Kristu ali yemweyo dzulo, ndi lero, ndi ku nthawi zones (Aheberi 13:8). Masiku ano tikumva ndi kuwerenga maumboni ambiririmbiri a machiritso odabwitsa omwe ali yankho la pemphero lachikhulupiliro.

Kodi mukuganiza kuti mwina sichingakhale chifuniro cha Mulungu kuti akuchiritseni? Baibulo limati fotokozera za munthu wina wakhate yemwe amaganiza chomwechi. Iye anati kwa Yesu, “Ambuye, ngati ndichifuniro chanu mundichiritse.” Yesu anamuyankha kuti, “Inde ndikufuna; chira.” Kuchokera pamenepa tingathe kuwona kuti Yesu ndiwofuna kuchiritsa masiku ano komanso nthawi zones. Zoon, machiritso kudzera m’mphamvu ya Mulungu ndi dalitso ndiponso mphatso ku moyo wa mkhristu. Nanga tsopano munthu akhoza kulandira bwanjali dalitsoli?

Nazi njira zinayi momwe mungathe kulandirira dalitso la machiritso ndi mphamvu ya Mulungu.

(1) Pemphero la chikhulupiliro lomwe adzapemphera akuluampingo. Yakobo akunena kuti “Pali wina kodi adwala mwa inu? Adziitanire akulu ampingo, ndipo

apemphere pa iye, atamdzozo ndi mafuta mdzina la Ambuye: ndipo pemphero la chikhulupiliro lidzapulumutsa wodwalayo ndipo Ambuye adzamuukitsa” (Yakobo 5:14,15). Tikagwiritsa ntchito njira imeneyi, pali ubwino wakuti chikhulupiliro cha akuluwampingo chimawonjezera pa chikhulupiliro cha wodwala uja. Njira imeneyi ndiyo imene amagwiritsa ntchito kawirikawiri aKhristu ambiri.

(2) Njira ina ndikugwirizana ndi wokhulupirira wina kuti mupempherere machiritso pa munthu wodwala. M’buku la Mateyu akunena kuti “Ngati awiri a inu avomerezana pansu pano chinthyu chiri chonse akachipempha, Atate wanga wakumwamba adzawachitira (Mateyu 18:18). Mgwirizano wamtundu umenewu mu pemphero umawonetsa chikondi chimene chimafunika kuwonetsedwa pa qulu la okhulupilira. Pemphero likakhala lochokera pa chikondi cha pa Mulungu li makhala lamphamvu komanso limakhala pemphero logwira ntchito yake moyenera.

(3) Njira yina yofanana ndi iyi ndikupemphererana wina ndi mnzake pakati paaKhristu. Yakobo woyera akutilimbikitsa motere “Ululani zolakwa zanu wina kwa mnzake, ndipo mupemphererane wina ndi mnzake kuti muchiritsidwe. Pamene pa aklukamba za anthu angapo odwala amene akhoza kupemphererani wina ndi mnzake kuti achiritsidwe. Nthawi zina kumakhala kosavuta kwa anthu oti ali mmavuto ofanana kuti amvane bwinobwino ndiponso kuti amverane chisoni. Komanso pakakhala pofunika kuti anthu anlule zolakwa zao wina kwa mnzake zomwe zimabwenzera m’mbuyo chikhulupiro chao, sipakhala vuto ngati anthu ali ndi zosowa zofanana. Chikhulupiliro cha anthu awiri pa kanthu ndichothandiza kwambiri.

(4) Pemphero lapawekha mudzina la Yesu liri ndi malonjezo ochuluka. Yesu anena motere kwa omtsatira ake “Ndipo chimene chiri chonse mukafunse m’dzina langa, ndidzachita, kuti Atate akalemekezedwe mwa Mwana. Ngati mudzapempha kanthu mdzina langa, ndidzachita” (Yohane 14:13,14). Pamene tipemphera kuti Mulungu atichiritse m’dzina la Yesu ndipo Mulungu akatichiritsa natimasula, izi

zimabweretsa ulemelero kwa Atate. Atate amalemekezedwa ndi mphamvu yakuwombola ndi kuchiritsa ya Mwana wake Yesu. Ndiponso Yesu ananena kuti “Zinthu ziri zones mukazipemphera ndi kuzipempha, khulupirani kuti mwazilandira, ndipo mudzakhala zao. (Izi ndizoona) Marko 11:24. Tikapemphera ndi chikhulupiliro, timakhulupirira kuti pemphero lathu layankhidwa pamene tikadapemphera ndipo timalandira dalit woli monga mphatso yopatsidwa nthawi yomweyo lyochokera ku chisoni cha Mulungu. Ngati muli pa nokha, imani nga-nga-nga pa lonjezo tanena m’mwambamu ndipo mukhulupirire kuti Ambuye adzakhala wokhulupirika m’malonjezo ake.

Takamba za njira zinayi za mmene mungalandirire machiritzo, ndipo mosakaika konse, pali njira zina zambiri. Mulungu ndiwachifundo potipatsa njira zambirimбири mmene tingafikire kwa Mchiritsi Wamkulu. Ndikudzi wa kuti Mzimu Woyera adzawonetsa aliyense wa ife njira yomwe ife tingatsate pomwe ife tidzafunitsitsa kuchiritsidwa ndi Mulungu. Dzisankhireni nokha wokondedwa njira zimene Ambuye wathu wachifundo wapereka kuti umunthu wathu wonse: thupi, moyo ndi mzimu ukawomboledwe kwathunthu.

Wokondedwa, ngati simunalandirebe Kristu kukhala mpulumutsi wanu, muitaneni tsopano lino m’chikhulupiliro Nthawi zambiri machiritso amabwera ngati machimo ako akhululukidwa.